Baibulo ya ana

Ikupasilani



Mfumu yanzeru Solomo

Yolembedwa ndi: Edward Hughes

Yojambulidwa ndi: Lazarus
Alastair Paterson

Yotengedwa ndi: Ruth Klassen

Yotathauzidwa ndi: Tapiwa Maraira

Yo pangidwa ndi: Bible for Children
www.M1914.org

©2022 Bible for Children, Inc.
Chilolezo: Muli ndi ufulu wotenga ndi kuchurukitsa makopewa koma osagulitsa.

Mfumu Davide anali munthu wamkulu wa Mulungu. Mu ulamuliro wake, Israyeli anakula kuŵirikiza nthaŵi khumi kuposa ufumu wa Mfumu Saulo. Koma tsopano sakanathanso kulamulira. Davide anali wokalamba.

Ndi kutopa!
Ndipo odwala!
Moyo wake padziko lapansi unali pafupi kutha.

Mmodzi wa ana ambiri a Davide, Adoniya,

anauza Aisrayeli kuti tsopano adzakhala mfumu. Ngakhale kuti dzina lake limatanthauza kuti "Mbuye wanga ndiye Mulungu," Adoniya sanali munthu wabwino. Iye anayesa kuba mpando wachifumu, podziwa kuti Davide anali wofooka kwambiri moti sakanatha kumukaniza. Koma Mulungu anali ndi zolinga zina!

Bateseba, mkazi wa Davide, anadziŵa kuti mwana wake Solomo ndiye ayenela kukhala mfumu. Iye anauza Davide zimene Adoniya anakonza. Ngakhale kuti anali kudwala, Davide anasonkhanitsa atsogoleri ake n'kumuika pamaso pa anthu kuti Solomo akhale mfumu ya Isiraeli.



Solomoni sanavutikenso ndi Adoniya chifukwa anthu a Isiraeli anakhulupirira Davide. Davide anawauza kuti Solomo ndi amene Mulungu anamusankha kuti akhale mfumu yawo. Pasanapite nthawi, Davide anamwalira.





Davide asanamwalire, analankhula ndi Solomo za kumvera Mulungu ndi kukhala mfumu yabwino. "Uyende m'njira za Mulungu, kuti ukachite bwino m'zonse uzichita," Davide anauza mwana wakeyo. Umenewo unali malangizo abwino! Kenako Solomo anakhala pampando wachifumu wa Davide bambo ake, ndipo ufumu wake unakhazikika.

Usiku wina, Solomo analota maloto. M'maloto ake, Mulungu anaonekera kwa iye n'kunena kuti: "Pempha kuti ndikupatse chiyani?" Kodi mukanapempha chiyani?

Solomo anapempha nzeru kuti akhale mfumu yabwino. Pempho la mfumu yachichepereyo linakondweretsa Mulungu. Solomo analandira zimene anapempha, koma Mulungu anamulonjezanso chuma chambiri ndi ulemu.

Sipanatenge nthawi kuti anthu adziwe nzeru za Solomo. Tsiku lina, amayi awiri anabwera patsogolo pake, ali ndi mwana mmodzi. "Mwana wa mayiyu anamwalira usiku, ndipo anasintha mwana wake wakufayo m'malo mwa wanga wamoyo," anatero mayi wina. "Ayi! Koma wamoyoyo ndiye mwana WANGA, ndi wakufayo ndiye mwana wako," anatero mayi winayo. Kodi mfumu ikanadziwa bwanji mayi weniweni?

Pamenepo mfumu inati, Ndibweretsereni lupanga. Ndipo anadza nalo lupanga pamaso pa mfumu. Choncho anabweretsa lupanga kwa mfumu. Kodi mukuganiza kuti mfumuyo inkafuna kuchita chiyani ndi lupanga?



Ndipo mfumu inati, Gawani pakati mwana wamoyoyo, ndi kumpatsa theka lina, ndi theka lina kwa wina. Kenako mayi wa mwana wamoyoyo anati, "O mbuyanga, mpatseni mwana wamoyoyu, ndipo Musamuphe ayi."

Koma winayo anati, Asakhale wanga kapena wanu, koma mumugawane.

Tsono mfumuyo inati,
“Patsani mkazi woyambayo
mwana wamoyoyo.
Ameneyo ndiye amake.”
Ndipo Aisrayeli onse
anamva za chiweruzocho,
nalemekeza kwambiri
mfumu. Anaona kuti nzeru
za Mulungu zinali mwa iye.

Aisiraeli analibe kachisi wolambiriramo Mulungu. Pamene Davide analinganiza kumanga imodzi, Mulungu anati, "Mwana wako ndiye adzamangira dzina langa nyumba."



Choncho Solomo anayamba kumanga kachisi wokongola kwambiri ku Yerusalemu.

Anatenga zaka 7 kuti amange kachisi. Koma tsiku lalikulu linafika pamene anthu onse anasonkhana kuti amvetsere Solomo akupatulira kachisi kwa Yehova.



Pambuyo pa pemphero lodabwitsa, mfumu ndi anthu mokondwera anapereka nsembe zikwi zambiri ndipo anakhala ndi phwando lalikulu
kwa milungu iwiri!

Zitatha izi, Mulungu anaonekeranso kwa Solomo ndipo anamulonjeza kuti adzamudalitsa iye ndi Aisiraeli akamamvera Yehova.

Koma n'zomvetsa chisoni kuti Solomo kapena Aisiraeli ankamvera Yehova nthawi zonse. Mfumuyo inakwatira akazi ambiri amene Mulungu sanafune kuti awakwatire. Akazi ake achikunja anatembenuzira mtima wake ku mafano; ndipo mtima wake sunali wogwirizana ndi Yehova Mulungu wake monga mmene unalili mtima wa Davide atate wake.

Pamene Solomo anataya mwaŵi wake kumvera Mulungu, mmodzi wa akapitawo ake dzina lake Yerobiamu anakumana ndi chokumana nacho chachilendo.



Mneneri anamuuza kuti Mulungu adzagawa ufumu wa Solomo ndipo Yerobiamu adzalamulira mafuko khumi mwa mafuko khumi ndi awiri. Nthawi yomweyo Yerobiamu anathawira ku Iguputo. Iye ankadziwa kuti Solomo akanamupha ngati akanakhalabe.



Kenako Solomo anamwalira. Mwana wake Rehobowamu anasonkhetsa anthu msonkho woipa kuposa Solomo. Mafuko khumi anapanduka - nasankha Yerobiamu kukhala mtsogoleri wawo. Ufumu waukulu wa Solomo unagawikana pakati, monga mmene mneneri wa Mulungu ananenera. Mulungu sangadalitse kusamvera!

Mfumu yanzeru Solomo

Nthano yochokera mu mau a Mulungu, Baibulo,

opezeka mu

1 Mafumu 1-12

"Polowela pa mau anu pamapasa kuwala."
Masalimo 119:130

Mapeto

Nthano iyi yamBaibulo imakamba za ubwino wa Mulungu yemwe anatipanga ndipo akufuna kuti mumdziwe iye.

Mulungu amadziwa kuti tima chita zoipa, zimene zimachedwa chimo. Chilango cha uchimo ndi infa, koma Mulungu anatikonda kwambiri ndipo anatuma mwana wake yekha, Yesu, kuzatifela pamtanda ndi kunzunzika chifukwa cha machimo anu. Ndipo anaukanso kwa akufa na pita kumwamba! Ngati ukukhulupirira Yesu mupempheni akukhululukileni machimo anu, azakukhululukirani! Adzabwera kukhala nanu, ndipo muzakhala naye kunthawi zonse.

Ngati mukukhulupirira kuti izi ndizoona, nenani ichi kwa Mulungu: Ambuye Yesu, ndikhulupirira ndinu mwana wa Mulungu, ndipo munakhala munthu kundifera ine machimo yanga, ndipo mulinso ndi moyo. Chonde, lowani mmoyo mwanga ndikundi khululukira machimo anga, kuti ndikhale ndi moyo watsopano, ndipo tsiku lina ndikakhale ndiinu muyaya. Ndithandizeni kukumverani ndi kukhala mwa inu ngati mwana wanu. Ameni.

Welenga Baibulo ndi kuyankula ndi Mulungu matsiku onse!
Johane 3:16